MBIRI YA KATIKISIMU WA BAIBULO
MBIRI YA CHIPANGANO CHATSOPANO MWACHIDULE

Achinyamata (Kalasi yachiwiri)
Buku lachiwiri la awiri

Lolembedwa ndi **Rev G.Vanden Berg**
Mkonzi ndi **J.J.Lim**
Wothathandizira wapadera ndi **David Higgs**

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **W. Chapasuka** komanso **A. Mkwinda**
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** komanso **Rev. Precious Kanyowa**

February 2011 edition

Copyright © Gratia Dei Sola Media

Mbiri ya Katikisimu Wa Baibulo- Mbiri ya Chipangano Chatsopano Mwachidule
(Achinyamata- Buku lachiwiri la Awiri)
Lolembedwa ndi **Rev G.Vanden Berg**
Mkonzi ndi **J.J.Lim**
Wothathandizira wapadera ndi **David Higgs**

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **W. Chapasuka** ndi **A. Mkwinda**
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** ndi **Rev. Precious Kanyowa**

Buku leni leni loyambilira limene anatanthauzira ndi Rev. G. Vanden Berg eni ake ndi a Prostestant Reformed Churches of America
Buku ili lakonzedwanso ndi Rev. J.J. Lim mu 2011 mothandizidwa ndi Pilgrim Covenant Church.

Chichewa version © 2012 Gratia Dei Sola Media
Lasindikizidwa ndi Grata Dei Sola Media
Blk 203B, Henderson Road , #07-07, Singapore 159546
Website: www.gdsmedia.org
Email: gdsmedia.sg@gmail.com

Palibe akuloledwa kusindikiza kapena kuchulukitsa buku ili ngakhale za mkatimu

Copyright © Gratia Dei Sola Media

Synod ya Evangelical Presbyterian Church (EPC) ku Malawi ndi ku Mozambique inavomereza mu chaka cha 2012 kuti bukuli lizigwiritsidwa ntchito mu mipingo yawo yonse.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

MAWU A MLEMBI

Buku ili linakonzedwa mogwirizana ndi maganizo a Sinodi ya Protestant Reformed Churches m'zaka za 1955-60 .Cholinga chake ndi kupereka maziko a chiphunzinso cha chikhristu kwa ana a zaka zisanu ndi zinayi (9) ndi khumi (10).

Maphunziro makumi awiri ndi asanu a buku ili ndi okhuza chipangano cha tsopano ndipo cholinga ndi kutsindika mfundo ndi kuika mwadongosolo Mawu. Ndi mobwereza pokutha maphunziro asanu, bukuli liphunzitsidwa kwa masabata makumi.

Buku ili ndilothandizana ndi buku la mbiri ya chipangano chakale mwachidule lokonzedwa ndi Prof.H.C.Hoeksema ndipo liyenera kutsatana ndi mabuku a chipangano chakale ndi chatsopano a achinyamata okulirapo.

Buku la ntchito lakonzedwa pofuna kuthandizira bukuli.

Mkozi akuyamikira thandizo la komiti yokonza buku la katikisimu ndi komiti ya Katekisimu yowonikanso pokonza bukuli kuti azigwiritsa m'matchalichi.

Ndipo malonjezano a Mulungu athandize kugwiritsa ntchito bukuli pophunzitsa moyenera ndikufetsa mbewu ya uzimu yokhazikika ya pangano la Mulungu.

- **G Vanden Berg**

MAWU A MKONZI

Kagwiritsidwe ntchito ka katikisimu wophunzitsira ana mu mpingo ndi njira ya bwino komanso yothandiza. Timabuku tatsopanoti tasindikizidwa kuti tipereke kukhazikika pa mfundo ndi mbiri za baibulo zomwe zikhoza kutipatsa maziko enieni a Katikisimu monga Katikisimu wa mfupi wa Westminister yemwe ndiovomerezeka pogwiritsa ntchito mu Pilgrim Convenant Church ndi mu Evangelical Presbyterian Church. Takonzamo zolakwika zina kuchokera ku buku loyamba komanso tawonjezera mayankho ena kuti zikhale zokwanira ndi mmene mafunso afunsidwira.

Ngati inu monga makolo muli ndi chikhulupiriro chogwiritsa ntchito Katikisimu ameneyu kuyambira pa chiyambi mupeza kuti pomafika pano mwana wanu adzakhala akutha kuwerenga Katikisimu payekha ndikuloweza mayankho mosavuta poyerekeza ndi mmene anayambira. Izi zili choncho sikungofuna kuti akhwime bongo wake ayi, koma adziyetsera kuchita. Mudzapeza kuti kuphunzitsa mwana wanu kuloweza Katikisimu ndi chinthu chosangalatsa mmoyo kusiyana ndi kale.

Koma tisamalitse kwambiri kuti machitidwe a Katikisimu amenewa chisakhale chizolowezi chabe cha pa sabata kamodzi , kapena kuloweza ndi kumakumbukira pa mtima. Koma chichitike mwa pemphero ndi chikhulupiriro ndi chiyembekezo kuti chiphunzitso ndi mfundo za m’baibulozi zikhazikike m’mitima mwawo ndi cholinga choti tsiku lina (ngakhale lero lomwe) zikule ndi kubereka zipatso mu ufumu wa Khristu. Choncho amayi onse alimbikitse ana amene akuphunzira poloweza posakhumudwa nao pamene alakwitsa kamba ka nthawi yochepayo. Ndipo abambo ayetsetse kuti ana awo amvetse chowona chimene alowezacho, ndipo aone phindu lake ndi chiani ku moyo wao wauzimu pomutsogolera kwa khristu kupyolera ku mfundo zomwe aloweza.

Ambuye adalitse kuyetsetsa kwathu pophunzitsa ana athuwa m’njira ya Mulungu.

- **J J Lim,June 2004**

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 1
KUBADWA KWA YOHANE M'BATIZI
Luka 1

1.Kodi Mulungu anatuma ndani kuti akonzekeletse njira ya Khristu?
Yohane M'batizi. (Luka 1:76-79; onaninso Yesaya 40:3; Mateyu 3:1-3)

2.Kodi makolo a Yohane m'batizi anali ndani?
Anali anthu owopa mulungu Zakaliya ndi Elizabeti. (Luka 1:5-13)

3.Kodi Baibulo limatiwuza chiani za kubadwa kwa Yohane?
Sanabadwe kufikira makolo ake atakalamba kwambiri. (Luka 1:7,18)

4.Kodi nchifukwa chiani Mulungu anadikira mpaka Zakaliya ndi Elizabeti anakalamba?
Kusonyeza kuti kubadwa kwa Yohane m'batizi ndi chisomo chachikulu (Luka 1:36-37)

5.Kodi kubadwa kwa Yohane m'batizi kunalengezedwa bwanji?
Mngelo Gabriel anamuuza Zakaliya mkachisi. (Luka 1:13-17)

6.Kodi Zakaliya anachita chiani m'kachisi muja?
Amagwira ntchito yopereka nsembe m'kachisi. (Luka 1:8-9)

7.Ndichizindikilo chanji chimene Zakaliya analandila chifukwa cha kusakhulupirira?
Sanathe kuyankhula za zodabwitsa zomwe mngelo Gabriel ananena. (Luka 1:19-20, 22)

8 Ndichifukwa chiani Zakaliya sanakhulupirira uthenga umene Zakaliya ananena?
Chifukwa onse awiri anali okalamba kwambiri. (Luka 1:18-20)

9.Kodi Mulungu analolanso Zakaliya kuyankhulanso?
Inde, pamene Zakaliya anatchula dzina la Yohane, Mulungu anamasulanso lilime ndipo ananenera. (Luka 1:63-79)

10.Kodi zikutanthauza chiani ponena kuti Yohane anali mnazili?
Kuti kuyambira pachiyambi Mulungu anampatula. (Luka 1:15; onaninso Numeri 6:1-8)

MAVESI OLOWEZA:
“Eya,ndipo iwetu kamwanawe, udzanenedwa mneneri wa Wamkulukulu: Pakuti udzatsogolera Ambuye, kukonza njira zache; Kuwapatsa anthu ache adziwitse chipulumutso, ndi makhalidwe a machimo ao (Luka 1:76, 77).

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 2.
KUBADWA KWA YESU NDI UMWANA WAKE
Luka 2, Mateyu 2

1.Ndani analengeza za kubadwa kwa Yesu kwa Maria?
Mngelo Gabriel yemwe analengezanso za kubadwa kwa Yohane m'batizi. (Luka 1:26)

2.Kodi Maria anali ndani?
Anali namwali yemwe samadziwa mwamuna wa fuko la Davide (Luka 1:27).

3.Kodi Ambuye Yesu anabadwira kuti?
Ku Betelehemu mu Mzinda wa Davide. (Mateyu 2:1; Luka 2:1-6)

4.Kodi woyamba kumva za kubadwa kwa Ambuye anali ndani?
Abusa omwe amaweta nkhosa ku tchire la ku Betelehemu. (Luka 2:8-10)

5.Ndichizindikiro chanji chimene abusa aja anapatsidwa?
"Mudzapeza mwana wakhanda wokuta ndi nsaru atagona modyera" (Luka 2:12)

6.Kodi Yosefe ndi Maria anamutengera kuti Ambuye Yesu pamene anali ndi masiku makumi anayi?
Kukachisi kukamupereka kwa Mulungu. (Lev 12:1-4, 6; Luka 2:21-24, 27)

7.Kodi Yosefe ndi Maria anakumana ndi ndani kukachisi?
Simioni wokalamba yemwe analosera ndipo anakondwera ndikubadwa kwa Yesu. (Luka 2:25-35)

8.Kodi anachokera ku mmawa ndani kudzamuona ndi kumuyamika Ambuye Yesu?
Anzeru a kummawa omwe anaona nyenyezi ndipo anafunsira kwa Herodi komwe kunabadwira kamwanako. (Mateyu 2:1-11)

9.Kodi Herodi anachita chiani pamene anzeru a kummawa sanabwere atampeza Yesu?
Anapha ana onse a mu Betrehemu omwe asanakwinitse zaka ziwiri zakubadwa. (Mateyu 2:16-18)

10.Atakwanitsa zaka khumi ndi ziwiri kodi Ambuye Yesu anapezeka kuti?
M'kachisi ku Yerusalemu akukhala pakati pa aphunzitsi namva iwo nawafunsa mafunso ovuta Komanso kuyankha mafunso amene amafunsidwa. (Luka 2:42-49)

MAVESI OLOWEZA: Luka 2: 7-14
"Ndipo iye anabala mwana wake wamwamuna woyamba; namkulunga iye m'nsaru, nam'goneka modyera ng'ombe, chifukwa kuti anasowa malo m'nyumba ya alendo……" Kwinako onani m'Baibulo.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 3
UTUMIKI WA YOHANE M'BATIZI
Luka 3:1-20; Mateyu 3:1-12

1.Kodi Yohane m'batizi anagwira ntchito yake kuti?
M’chipululu kufupi ndi mtsinje wa Yorodani. (Mateyu 3:1-6; Luka 3:2-3, 7)

2.Kodi Yohane amadya ndikuvala chiani?
Amadya dzombe ndi uchi ndipo amavala chovala choyera cha bweya wa ngamira. (Mateyu 3:4)

3.Kodi ntchito ndi maitanidwe a Yohane inali yotani?
Analalikira ndi kubatiza. (Luka 3:3-6,16)

4.Kodi Yohane amalalikira chiani?
Anawauza anthu kuti alape ndikuti ufumu wakumwamba wayandikira. (Mateyu 3:1-2, 7-11; Luka 3:7-8)

5.Kodi anthu ambiri anakhulupirira uthenga wa Yohane?
Inde, anthu ambiri anakhulupirira ndipo anabatizidwa. (Mateyu 3:5-6)

6. Ndi ndani anabwera kwa Yohane M’batizi pofuna kudziwa iye?
Mthumwi ya a Farisi ndi Asaduki ochokera ku Yerusalemu. (Mateyu 3:7)

7.Kodi Yohane anamufotokoza bwanji Yesu pa tsiku lotsatira?
“Onani Mwanawankhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo lake la dziko lapansi” (Yohane 1:29)

8.Kodi Yohane anawalimbikitsa omutsatira kuti achite chiani?
Kuti achoke kwa iye ndikusatira Ambuye Yesu. (Yohane 1:29-40)

9.Kodi pambuyo pake Ambuye Yesu ananena chiani zokhuza Yohane m'batizi?
Ananena kuti Yohane anali opambana kuposa aneneri onse a chipangano chatsopano. (Mateyu 11:7-11; Luka 7:24-28)

10.Kodi Herodi woipa uja anachita chiani pamene Yohane anamuzuzula iye za tchimo limene anachita?
Anamuika Yohane mbatizi mu ndende. (Luka 3:18-20)

VESI LOLOWEZA:
“Yohane anayankha ,nanena kwa onse, Inetu ndikubatizani inu ndi madzi; koma wakundiposa ine mphamvu alikudza, amene sindiyenera kumasula lamba la nsapato zache; Iyeyu adzakubatizani inu ndi Mzimu Woyera ndi moto; (”Luka 3:16)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 4
KUBATIZIDWA KWA YESU NDI KUYESEDWA KWAKE
Mateyu 3:13 – 4:11

1.Kodi Yesu anali ndi zaka zingati pamene Iye amayamba utumiki wake?
Anali ndi zaka makumi atatu (30) zakubadwa. (Luka 3:21-23)

2.Kodi Yesu anayamba bwanji utumiki wake?
Anapita ku mtsinje wa Yorodani kukabatizidwa ndi Yohane. (Mateyu 3:13-15)

3.Chinachitika ndi chiani Yesu atabatizidwa?
Kumwamba kunatseguka ndipo mzimu woyera unatsika pa Iye ngati nkhunda. (Mateyu 3:16-17; Mariko 1:8-11)

4.Kodi mawu ochokera kumwamba ananena chiani?
“Uyu ndiye mwana wanga okondedwa,mwaiyeyu ndikondwera” (Mateyu 3:17)

5.Chinachitika ndi chiani Yesu atangobatizidwa?
Mzimu woyera unatengera Yesu kuchipululu kukayetsedwa ndi satana. (Mateyu 4:1)

6.Kodi satana ndi ndani?
Iye ndi mfumu ya angelo oponyedwa kuchokera kumwamba,wotchedwa satana. (Chivumbulutso 12:9; 2 Petro 2;4; Yuda 6)

7.Kodi Ambuye Yesu anakhala masiku angati m'chipululu?
Anakhala ku chipululu kwa masiku makumi anayi usana ndi makumi anayi usiku (40) osadya ngakhale kumwa. (Mateyu 4:2)

8.Kodi satana anayesa Yesu kangati ku chipululu kuja?
Katatu m'malo atatunso osiyana. (Mateyu 4:3-10)

9.Kodi Ambuye Yesu anamvera satana?
Ayi, ananena, “Pita uko, satana” (Luka 4:8)

10.Anabwera kwa Yesu ndani atatha kuyetsedwa ?
Mngelo anabwera namtumikira Iye. (Mateyu 4:11)

VESI LOLOWEZA:
“Pakuti sitiri naye mkulu wa ansembe wosatha kumva chifundo ndi zofoka zathu; koma wayetsedwa m'zonse monga momwe ife, koma wopanda uchimo. (Ahebri 4:15)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 5
KUYAMBA KWA UTUMIKI WA AMBUYE YESU
Yohane 1:35 – 3:36

1.Kodi utumiki wa Ambuye Yesu unatha nthawi yayitali bwanji?
Pafupifupi zaka zitatu ndi theka

2.Kodi chimodzi mwa zinthu zoyambirira chimene Ambuye Yesu anachita ndi chiani?
Anasankha ophunzira ake.

3.Kodi ena mwa ophunzira ake ndi ndani?
Andreya, Yohane, Petulo, Filipo, Nataniel. (Yohane 1:35-46; Mateyu 4:18-22)

4.Chinachitika ndi chiani ku ukwati wa ku Kana?
Ambuye Yesu anachita chozizwa choyamba pamene anasandusa madzi kukhala vinyo. (Yohane 2:1-11)

5.Kodi Ambuye Yesu anapita kuti atachoka ku ukwati?
Anapita ku Kapernao kwa masiku ochepa kenako anapita ku Yerusalemu. (Yohane 2:12-13)

6.Kodi Ambuye anachita chiani ku Yerusalemu?
Anawathamangitsa anthu ogulitsa ndi ogula malonda a nyama zoperekera nsembe mkachisi (Yohane 2:14-16)

7.Kodi Yesu anawauza chiani anthu omwe anafunsa za chizindikiro cha udindo wake popanga zimenezo?
“Onongani kachisi uyu ndipo mmasiku atatu ndizamuzusa” (Yohane 2:19).

8.Kodi anabwera kwa Yesu usiku ndi ndani?
Nikodemo yemwe anali mfalisi ndi wolamulira wa Ayuda. (Yohane 3:1-2)

9.Kodi Ambuye anamuuza chiani Nikodemo?
“ Ngati munthu sabadwanso mwa tsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu. (Yohane 3:3)

10.Kodi Yohane anadandaula pamene anthu anayamba kusiya iye ndikutsatira Ambuye Yesu?
Ayi,ndipo ananena kuti,”Iyeyo ayenera kukula koma ine ndichepe.” (Yohane 3:30)

VESI LOLOWEZA:
'Iye amene akhulupirira mwanayo ali nao moyo wosatha; koma iye amene sakhulupirira Mwanayo sadzaona moyo, koma mkwiyo wa Mulungu ukhala pa iye. (Yohane 3:36)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 6
KUSAMARIA NDI GALILEYA
Yohane 4 ndi Luka 4:16 – 5:11

1.N'chifukwa chiani Ambuye Yesu anadzera ku Samaria popita ku Galileya?
Amafuna ayankhule ndi mzimayi wa ku Samaliya pa chitsime cha Yakobo. (Yohane 4:3-24)

2.Kodi Ambuye Yesu anamuuza chiani mzimayi waku Samariya?
Anamuuza kuti Iye ndi Mesiya wolonjezedwayo. (Yohane 4:25-26)

3.Kodi Ambuye analalikiranso kwa Asamaliya ena?
Inde, ambiri anabwera kudzamva Iye ndipo anakhulupirira kuti iye ndi Khristu. (Yohane 4:28-30, 39-42)

4.Kodi Ambuye Yesu analandiridwa ku Galileya?
Inde, chifukwa agalileya ambiri anaona zozizwa zake ku Yerusalemu? (Yohane 4:43-45)

5.Kodi Ambuye Yesu anachita chodzizwa chanji ku Kana wa ku Galileya?
Anachiza mwana wa mkulu yemwe amadwala ku Kaperenao. (Yohane 4:46-54)

6.Kodi Ambuye anaphunzitsa chiani m'sunagogi wa ku Nazareti?
Anaphunzitsa kuchokera m’malemba kuti Iyedi ndi Khristu. (Luka 4:16-21)

7.Kodi anthu amtundu wake anakhulupirira Iye?
Ayi, anamukana Iye ndipo anafuna kumupha. (Yohane 4:28-29)

8.Kodi Ambuye Yesu anapita kuti atachoka ku Nazareti?
Ku Kaperenao kumene analalikira ndi kuchita zodabwitsa. (Yohane 4:30-41; Mariko 1:31-42)

9.Kodi Ambuye anachita chiani pa nyanja ya Galileya?
Anachita chozizwa chapadera chogwira nsomba zambiri. (Luka 5:2-7)

10.Kodi Ambuye anachita chiani pa nthawi imene amachita zodabwitsa?
Anaitana ophunzira kuti asiye makoka awo ndikumulondola Iye. (Luka 5:8-11)

MAVESI OLOWEZA:
”Mzimu wa Ambuye uli pa Ine, Chifukwa chake Iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino. Andituma Ine kululikira a m'nsinga mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyenso, Kutulutsa ndi ufuru ophwanyika. Kulalikira chaka chosankhika cha Ambuye. (Luka 4:18,19)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 7
UTUMIKI WA KU GALILEYA
Yohane 5 ndi Mateyu 5 – 10

1.Ndi chifukwa chiani Ambuye Yesu anachoka ku Galileya kwa kanthawi?
Amafuna akakhale nao pa phwando la Ayuda ku Yerusalemu. (Yohane 5:1)

2.Kodi Ambuye Yesu anachita chiani pa thamanda la Betisaida?
Anachiza munthu opuwala tsiku la sabata. (Yohane 5:2-9)

3.Kodi chozizwa chimenechi chinakhuza bwanji Ayuda?
Anakwiya kwambiri ndipo anazuzula Yesu kamba ka kuswa sabata. (Yohane 5:10-16,18)

4.Kodi ndizoona kuti Ambuye Yesu anaswa sabata?
Ayi, chifukwa amachita zabwino pa sabata. (Yohane 5:17,19-23)

5.Kodi ndi chiphunzitso chanji chimene Yesu analalikira atabwerera ku Galileya?
Chiphunzitso cha pa phiri. (Mateyu 5 – 7)

6.Kodi mutu weniweni wa chiphunzitso chake chinali chotani?
Ufumu wa kumwamba, zizindikiro zake ndi madalitso a mzika. (monga Mateyu 5:3-11)

7.Kodi Ambuye Yesu anachiza ndani ku Kaperenao patangopita nthawi pang'ono?
Kapolo wa Kentuliyo yemwe anaonetsa chikhulupiriro chachikulu. (Mateyu 8:5-13)

8.Kodi ndichozizwa chachikulu chanji chimene Ambuye anachita ku Nayini patangotha masiku awiri?
Anaukitsa mwana wakufa wa mkazi wamasiye . (Luka 7:11-35)

9.Anabwera kwa Ambuye Yesu ndani pa nthawi imeneyi?
Ophunzira ena awiri a Yohane m'batizi omwe anamufunsa ngati analidi Khristu. (Mateyu 11:1-6)

10.Kodi Yohane M'batizi anafa bwanji?
Anadulidwa mutu ndi Herodi Antipasi. (Mateyu 14:3-12)

MAVESI OLOWEZA:
“Odala ali osauka mumzimu; chifukwa uli wao Ufumu wa Kumwamba. Odala ali achisoni; chifukwa adzasangalatsidwa. Odala ali akufatsa;chifukwa adzalandira dziko lapansi. Odala ali akumva njala ndi ludzu la chilungamo; chifukwa adzakhuta. Odala ali akuchita chifundo; chifukwa adzalandira chifundo. Odala ali oyera mtima;chifukwa adzaona Mulungu. Odala ali akuchita mtendere; chifukwa adzatchedwa ana a Mulungu. (Mateyu 5:3-9)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 8
ULENDO WACHIWIRI WA KU GALILEYA
Mateyu 11 – 13 ndi Luka 7 – 8

1.Kodi ndi chiphunzitso chanji chimene Ambuye Yesu amagwiritsa ntchito pa ulendo wake wachiwiri wa ku Galileya?

Amaphunzitsa m'zifanizo. (Mateyu 13:3a)

2.Kodi zifanizo ndi chiani?

Ndimaphiphiritso a dziko lapansi zomwe zimathandizira kuphunzitsa zoonadi za kumwamba. (Mateyu 13:10-17)

3.Tchulani zifanizo ziwiri zoyambirira zomwe Yesu anazinena?

Fanizo la wofetsa ndi nthaka, ndi fanizo la tiligu ndi nansongole. (Mateyu 13:3-9, 18-23; Mateyu 13:24-30, 37-42)

4.Ndi chifukwa chiani Yesu ananena za chiweruzo zamizinda itatu ya, Kapernao, Korazini ndi Betsaida?

Chifukwa anagwira ntchito yamphamvu m'midzi imeneyi,koma anthu sanakhulupirire. (Mateyu 11:20-24)

5.Kodi anabwera kwa Yesu ndani pamene Iye anali kudya kunyumba kwa Simon Mfalisi?

Mzimayi wochimwa yemwe anadzoza mapazi a Yesu ndi misonzi yake. (Luka 7:36-39)

6. Ndichifukwa chiani mzimayi wochimwa uja anadzoza mapazi a Yesu?

Kusonyeza chikondi ndi kuthokoza kwa Iye chifukwa machimo ake anakhululukidwa. (Mateyu 7:40-48)

7.Chinachitika ndi chiani pamene Ambuye Yesu ndi ophunzira ake anali kuoloka nyanja ya Galileya?

Namodwe wamkulu anabuka pa nyanja pamene Yesu anali kugona m'ngalawa. (Mateyu 8:22-23)

8.Kodi Ambuye Yesu anawonetsa bwanji mphamvu ndi udindo wake?

Analetsa namondwe ndipo anawazuzula ophunzira ache chifukwa chosowa chikhulupiriro. (Mateyu 8:24-25)

9.Ndichozizwa chanji chimene Yesu anachita tsidya lina la nyanja?

Anthu awiri odzala ndi mizimu yoipa anachiritsidwa ndipo mizimu yoipayo anailamulira kuti ilowe mu gulu la nkhumba. (Mateyu 8:28-32)

10.Kodi Ambuye Yesu anaukitsa kwa akufa ndani ku Kaperenawo?

Mwana wa mkazi wa Yairo. (Luka 8:41-42, 49-56)

MAVESI OLOWEZA:

“Idzani kuno kwa ine nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo ine ndidzapumulitsani inu; Senzani gori langa, ndipo phunzirani kwa Ine chifukwa ndiri wofatsa ndiwodzichepetsa mtima; ndipo muzapeza mpumulo wa miyoyo yanu. Pakuti gori langa liri lofewa, ndi katundu wanga ndi wopepuka” (Mateyu 11:28-30)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 9
ULENDO WACHITATU WA KU GALILEYA
Yohane 6 ndi Mariko 6 – 8

1.Ndi chifukwa chiani Ambuye Yesu anatumiza ophunzira khumi ndi awiri?
Kukalalikira Uthenga Wabwino ndikuchiza odwala. (Mariko 6:7-13)

2.Kodi Yesu anapita kuti pamene anamva za imfa ya Yohane M'batizi?
Anapita kuchipululu mbali ina ya nyanja ya Galileya . (Mariko 6:16-31; Mateyu 14:1-13)

3.Kodi ndi chozizwa chanji chimene Ambuye Yesu anachita kufupi ndi Kapernao?
Anadyetsa anthu opitirira mazana asanu (5000) ndi mikate isanu ndi tinsomba tiwiri. (Mariko 6:34-44; Yohane 6:5-14)

4.Kodi chotsatira chodyetsa anthu mazana asanu aja chinali chiani?
Anthu anafuna kumpanga Yesu kuti akhale mfumu yao. (Yohane 6:15)

5.Kodi Ambuye Yesu amafuna kuti akhale mfumu yao?
Ayi, chifukwa ufumu wake ndi wakumwamba osati wa dziko. (Yohane 6:36-41; 18:36)

6.Kodi anthu amutsatabe Yesu pamene Iye sangakhale mfumu yao?
Ayi, anamusiya Iye ndipo sanamutsatenso. (Yohane 6:66)

7.Kodi Petro ananena chiani pamene Ambuye anafunsa ophunzira ngati iwonso akufuna kumuchokera?
Petro anati," Ambuye tidzamuka kwa yani? Inu muli nao mau a moyo wosatha. (Yohane 6:68)

8.Ndi chozizwa chanji chimene Ambuye Yesu anachita ku Turo ndi ku Sidoni?
Anachiza mwana wa mkazi wa Msuro- Fonika yemwe anali ndi chikhulupiriro chachikulu. (Mariko 7:24-30)

9.Kodi mzimayi wa ku Msuro-Fonika anaonetsa bwanji chikhulupiriro chake?
Anabvomereza kuti iye ali ngati galu pansi pa gome namadyako nyenyeswa za ana. (Mariko 7:27-28)

10.Kodi ndichozizwa chanji chimene Ambuye anachita ku Dekapoli?
Anachiza munthu osamva ndi osayankhula. (Mariko 7:31-35)

VESI LOLOWEZA:
Yesu anayankha, "Ufumu wanga suli wa dziko lino lapansi; ufumu wanga ukadakhala wa dziko lino lapansi, anyamata anga akadalimbika nkhondo, kuti ndisaperekedwe kwa Ayuda; koma tsopano ufumu wanga suli wochokera konkuno (Yohane 18:36).

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 10
MAWALISIDWE A YESU PA PHIRI
Mateyu 16 – 17; Luka 9 ndi Yohane 10

1.Kodi Ambuye anayamba kuwauza chiani ophunzira ake pamene amatsiriza utumiki wake?
Anawauza zoti Iye adzamva zowawa ndikufa m'Yerusalemu ndipo adzauka tsiku la chitatu. (Mateyu 16:21; 17:9, 12; Luka 9:21-22, 44)

2.Kodi Petro ananena chiani za Ambuye pamene anali ku Kaisaleya wa filipi?
"Inu ndinu khristu Mwana wa Mulungu wa moyo." (Mateyu 16:16)

3.Kodi Ambuye Yesu anapita kuti Petro atalapa kwa thunthu ?
Anapita ku phiri ndi atatu mwa ophunzira ache. (Mateyu 17:1; Luka 9:28)

4.Kodi chinachitika ndi chiani pamene Yesu anali kupemphera pa phiri?
Anasanduka pamaso pa ophunzira ache. (Mateyu 17:2; Luka 9:29)

5.Kodi Yesu anayankhulana ndi ndani pamene anali kusandulika pa phiri paja?
Mose ndi Eliya omwe anayankhula ndi Ambuye za mazunzo ndi imfa yake. (Mateyu 17:3; Luka 9:30-31)

6. Chifukwa chiani ophunzira anakangana?
Anali kukangana kuti mwa iwowo wamkulu mu ufumu wa kumwamba ndi ndani? (Luka 9:46-48)

7.Kodi ndi mgonelo wa Ayuda uti umene Yesu anapita pa nthawi imeneyi?
Anapita ku phwando m'kachisi ku Yerusalemu. (Yohane 7:1-14)

8.Ndi chifukwa chiani Afalisi anakwiya ndi Ambuye Yesu pa tsiku la sabata litatha phwando la m'kachisi?
Anachiza munthu osaona tsiku la sabata. (Yohane 9:13-16)

9.Kodi Ambuye anaphunzitsa chiani zokhuza Iye mwini lisanafike phwando lakukonzetsanso?
Kuti Iye ndi m'busa wabwino yemwe anapereka moyo wake chifukwa cha nkhosa zake. (Yohane 10:1-18)

10.Kodi Iye anawauza chiani Ayuda osakhulupirira?
'koma inu simukhulupirira,chifukwa simuli mwa nkhosa zanga" (Yohane 10:26)

MAVESI OLOWEZA;
' Pakuti analandira kwa Mulungu Atate ulemu ndi ulemerero, pakumdzera Iye mau otere ochokera ku ulemerero waukuru ,Uyu ndi Mwana wanga wokondedwa, umene Ine ndikondwera naye; Ndipo mau awa ochokera Kumwamba tidamva ife, pokhala pamodzi ndi Iye m'phiri lopatulika lija? (2 Petro 1:17,18)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 11
CHIUKITSO CHA LAZALO
Yohane 10 – 11 ndi Luka 18 – 19

1.Kodi Ambuye Yesu anapita kuti atatha phwando la kukonzetsanso?

Anapita ku Pereya tsidya lina la nyanja ya Yordano kumene anthu ambiri anakhulupirira Iye. (Yohane 10:39-42)

2. Ndi uthenga wotani unabwera kwa Yesu pamene Iye anali ku Pereya?

Anauzidwa kuti mnzake Lazalo anadwalika kwambiri. (Yohane 10:40 – 11:3)

3.Kodi Ambuye Yesu anapita ku Betania kukachiza Lazalo nthawi yomweyo?

Ayi, anadikira mpaka Lazalo atamwalira. (Yohane 11:5-7, 11-14, 17, 32-36)

4.Ndi chifukwa chiani Ambuye Yesu anadikira mpaka Lazalo anamwalira?

Kuti aonetse mphamvu zake pomuukitsa Lazalo ku imfa. (Yohane 11:14-15, 39-44)

5.Kodi zotsatira za chozizwa chachikulu chimenechi ndi chiani?

Anthu ambiri anakhulupirira koma atsogoleri oipa anapanga upo kuti amuphe Yesu. (Yohane 11:45-53)

6.Kodi Ambuye Yesu anapita kuti pamene atsogoleri anapanga upo kuti amuphe Yesu?

Kumudzi wotchedwa Eferemu komwe anakhala masabata otsiriza a utumiki wake. (Yohane11:54 – 12:1)

7.Kodi Ambuye anamuuza chiani mdindo mwini chuma yemwe anabwera kufuna moyo osatha?

'Ngati ufuna kukhala wangwiro, kagulitse zomwe uli nazo, nupatse aumphawi. (Mateyu 19:21)

8.Kodi ndichozizwa chanji chimene Ambuye anachita atayandikira Yeriko?

Anachiza Batumeyo wakhungu. ((Luka 18:35-43; Mariko 10:46-52)

9.Anakwera mumtengo ndi ndani kuti awone Ambuye?

Zakeyu wa nsonkho amene kunyumba kwake Ambuye anabweretsa chipulumutso. (Luka 19:1-10)

10.Kodi Maria m'bale wake wa Marita ndi Lazaro anachita chiani ku Betaniya?

Anamudzoza Ambuye Yesu ndi mafuta onunkhira bwino a mtengo wa patali kukonzekera kuikidwa m'manda. (Yohane 12:3-8)

MAVESI OLOWEZA:

“Yesu anati kwa iye, Ine kuuka ndi moyo : wokhulupirira Ine angakhale amwalira, adzakhala ndi moyo; Ndipo yense wakukhala ndi moyo, nakhulupirira Ine, sadzamwalira nthawi yonse. (Yohane 11:25,26)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 12
SABATA YA MASAUTSO
Luka 19 – 22 ndi ndime zina

1.Ndichaka chiti chimene Ambuye Yesu anapachikidwa?
Mchaka cha 33 A.D.

2.Kodi Ambuye Yesu anachita chiani pa tsiku loyamba la sabata imene anapachikidwa?
Anakwera pa mwana wa bulu ndi kulowa mu Yerusalemu. (Luka 19:29-38; Mateyu 21:7-12)

3.Kodi anthu omusatira Ambuye Yesu anafuula bwanji?
“Osana kwa mwana wa Davide.” (Mateyu 21:9)

4.Kodi Ambuye Yesu anachita chiani mkachisi muja tsiku lolemba?
Anathamangitsa anthu omwe anayesa nyumba ya Atate wake nyumba ya achifwamba. (Luka 19:45-46)

5.Kodi Ambuye anachita chiani panjira ya ku Betaniya m'mawa wa tsiku lolemba?
Anatemberera mkuyu osabereka. (Mateyu 21:18-21; Mariko 11:12-14, 19-22)

6.Kodi Ambuye Yesu anachita chiani pa tsiku lachiwiri?
Anaphunzitsa anthu kwa nthawi yotsiriza. (Luka 20:1)

7.Kodi Ambuye analosera chiani pa tsiku la chiwiri madzulo?
Ananena za kupasuka kwa Yerusalemu ndi kubweranso kwake kwachiwiri. (Luka 21:5-37; onaninso Mateyu 24:4 – 25:13)

8.Kodi Ambuye anakhala motani tsiku lachitatu la sabata yotsiriza?
Anali yekha ndi ophunzira ake yemwe anawauza za imfa yake. (Mateyu 26:1-2)

9.Kodi Yudasi Esikaliyoti anachita chiani pa tsiku la chitatu?
Anavomereza kumpereka Ambuye Yesu ndi makobili makumi atatu a siliva. (Luka 22:1-6; Mateyu 26:14-16; Mariko 14:10-11)

10.Ndichifukwa chiani Yudasi anapereka Ambuye Yesu?
Chifukwa Yudasi anali ochimwa ndipo satana analowa mumtima mwake. (Luka 22:3; Yohane 6:70-71)

VESI LOLOWEZA:
“Pakuti kunamuyenera Iye amene zonse ziri chifukwa cha Iye, ndi zonse mwa Iye, pakutenga ana ambiri alowe mwa Iye, pakutenga ana ambiri alowe ulemerero, kumkonza wamphumphu mtsogoleri woyamba wa chipulumutso chao mwa zowawa.” (Ahebri 2:10)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 13
KUMANGIDWA NDI KUZENGEDWA KWA AMBUYE YESU
Mateyu 26 – 27 ndi Yohane 18

1.Kodi Ambuye Yesu anachita chiani pa tsiku lachinayi sabata yake yotsiriza?
Anadya mgonero otsiriza ndi ophunzira ake pa chipinda cha pamwamba. (Mateyu 26:17-25; Luka 22:10-12)

2.Kodi Ambuye Yesu anachita chiani kwa ophunzira ache ali pa chipinda cha pamwamba?
Anasambisa mapazi monga amachira kapolo. (Yohane 13:2-17)

3.Kodi Ambuye Yesu anachita chiani atatha kudya pasaka ndi ophunzira ake?
Anakhazikitsa Mgonero wa Ambuye. (Mateyu 26:26-29)

4.Kodi Ambuye Yesu anapita kuti ndi ophunzira ake atachoka pa chipinda cha pamwamba?
Anapita kumunda wa Getsemani komwe Iye anapemphera ophunzira ake akugona. (Mateyu 26:36-46)

5.Kodi anabwera m'munda muja ndi ndani kudzamugwira Ambuye Yesu?
Yudasi Esikarioti ndi gulu lalikulu ndi ansembe akuru. (Mateyu 26:46-50)

6.Kodi anthu aja akanatha kumugwira Ambuye?
Ayi, kufikira Ambuye anadzipereka yekha. (Yohane 18:1-8)

7.Kodi ophunzira aja anachita chiani pamene Ambuye Yesu anagwidwa?
Anamusiya Iye nathawa. (Mateyu 26:56)

8.Kodi adani a Ambuye Yesu anamutengera kuti poyamba?
Kwa akuru a Ayuda kuti akamuzenge mulandu. (Mateyu 26;57; Yohane 18;12-14)

9.Kodi Petro anachita chiani pamene Ambuye Yesu anali kuzengedwa?
Anamukana Ambuye katatu. (Mateyu 26:69-75; Yohane 18:16-18, 25-27)

10.Kodi amene anamuweruza Yesu ndani kuti aphedwe?
Pontio Pilato ,kazembe wa ku Roma. (Mateyu 27:1-2,11-24)

VESI LOLOWEZA:
"Ndipo anamuka patsogolo pang'ono, nagwa nkhope yache pansi, napemphera,nati , Atate, ngati nkutheka, chikho ichi chindipitirire Ine; koma si monga ndifuna Ine, koma Inu. (Mateyu 26:39)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 14
KUPACHIKIDWA KWA AMBUYE YESU
Luka 23 ndi Yohane 19

1.Kodi Pilato anasonyeza bwanji kuti iye anali oweruza ofowoka?

Ngakhale anadziwa kuti Ambuye Yesu analibe tchimo, iye anaweruza kuti Iye akaphedwe. (Luka 23:1-25)

2.Kodi Yudasi Esikariot anachita chiani atamupereka Yesu?

Anabweza ndalama ija kwa wa mkulu wa nsembe ndipo anachoka kukazimangirira. (Mateyu 27:3-10)

3.Kodi Ambuye Yesu anapachikidwa kuti?

Pa phiri la Gologata kunja kwa Yerusalemu. (Yohane 19:16-18)

4.Ndi chifukwa chiani Yesu anafa imfa ya pa mtanda?

Kuti apulumutse anthu ake kumachimo awo. (Mateyu 1:21; onaninso 1 Petro 2:24-25)

5.Kodi Yesu anapachikidwa ndi yani?

Ndi amuna awiri okuba. (Luka 23:32-33)

6.Kodi mmodzi mwa opalamula aja anamuuza chiani Yesu?

“Ambuye , mukumbukire ine pamene mukulowa mu ufumu wanu”. (Luka 23:42)

7.Kodi Ambuye anamuuza chiani olapa opalamula uja?

“Lero lino udzakhala ndine m'Paradizo”. (Luka 23:43)

8.Kodi Ambuye ananena chiani Iye asanafe?

“Atate, m'manja mwanu ndipereka mzimu wanga” (Luka 23:46)

9.Chinachitika ndi chiani pa nthawi imene Ambuye Yesu amafa?

Chinsalu cha mkachisi chinang'ambika pakati, kunamveka chivomerezi ndipo manda a anthu akufa anatseguka. (Mateyu 27:51-53)

10.Kodi anaika mmanda thupi la Ambuye Yesu ndi ndani?

Anaika ndi Yosefe wa ku Arimateya . (Luka 23:50-53; Yohane 19:38-42)

VESI LOLOWEZA:

“Koma kudzitamandira ine konse konse, iai, koma mu mtanda wa Ambuye wathu Yesu Kristu, amene mwa Iye dziko lapansi lapachikidwira ine, ndi ine ndapachikiridwira dziko lapansi” (Agalatiya 6:14)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 15
YESU AUKA KWA AKUFA
Mateyu 28; Yohane 20 ndi Luka 24

1.Kodi chinachitika pa tsiku loyamba la sabata yakuwuka mmanda ndi chiani?

Ambuye Yesu anauka kwa akufa monga mmene Iye ananenera. (Mateyu 28:1-6; Luka 24:1-6; Yohane 20:1, 11-16)

2.Kodi Amayi amene anapita kumanda kukazonda mtembo wa Yesu anapeza chiani?

Anapeza kuti mwala wotsekera pa manda unakunkhunizidwa, ndipo mmanda munalibe. (Mateyu 28:1-6; Luka 24:1-6; Yohane 20:1, 11-16)

3.Kodi anawauza amayi za kuuka kwa akufa ndi ndani?

Angelo omwe anakhala pa mwala womwe unakunkhunizidwa pa manda. (Mateyu 28:2,4)

4.Kodi akuru a Ayuda anakana bwanji za kuuka kwa Yesu?

Anafalitsa mbiri yoti ophunzira anabwera ndi usiku ndipo anaba mtembo wa Ambuye Yesu? (Mateyu 28:11-15)

5.Kodi Ambuye Yesu poyamba anaonekera kwa ndani atauka mmanda?

Kwa Mariya Magadala ku manda. (Yohane 20:11-16)

6.Kodi Iye anaonekeranso kwa ndani patangotha izi?

Kwa akazi omwe anali kuchokera kumanda? (Mateyu 28:5, 8-10)

7.Kodi Ambuye Yesu anaonekera kwa ndani tsiku lomweli zitapita izi?

Kwa Petro ndi ophunzira awiri omwe anali paulendo wa ku Emau. (Luka 24:13-31, 33-34; 1 Akorinto 15:3-6)

8.Kodi Tomasi ananena chiani pamene anamva zoti Ambuye Yesu wauka?

Ananena kuti sangakhulupirire kufikira iye mwini atamuona Yesu. (Yohane 20:24-29)

9.Ndi nthawi yaitali bwanji pamene Ambuye Yesu anaonekera kwa ophunzira atauka kwa akufa?

Kwa masiku makumi anayi. (40) (Machitidwe a Atumwi 1:1-3)

10.Ndi chifukwa chiani Ambuye Yesu amaonekera kwa ophunzira ache kwa masiku makumi anayi amenewa?

Kuwaphunzitsa ophunzira ache zinthu zambiri zokhuza ufumu wa kumwamba. (Machitidwe Atumwi 1:3)

MAVESI OLOWEZA:

“Koma tsopano Kristu waukitsidwa kwa akufa, chipatso choundukula cha iwo akugona. Pakuti monga imfa inadza mwa munthu, kuuka kwa akufa kunadzanso kwa munthu. Pakuti monga mwa Adamu onse omwalira, choterenso mwa Khristu onse anakhalitsidwa ndi moyo” (1 Akorinto 15:20-22)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 16
KUKWERA KUMWAMBA NDI PENTEKOSTE
Machitidwe a Atumwi 1 ndi 2

1.Chinachitika ndi chiani patatha masiku makumi anayi Ambuye Yesu atauka m'manda?
Yesu anatengedwa kunka kumwamba ophunzira ake akumuona. (Machidwe 1:1-3)

2.Kodi Ambuye Yesu analonjeza chiani ophunzira ache pamene anali kupita kumwamba?
Iye adzadza momwemo monga munamuona alikupita kumwamba. (Machitidwe 1:9-11)

3.Kodi ophunzira anachita chiani Yesu atakwera kunka kumwamba?
Anapita ku Yerusalemu kukadikirira kudzodza kwa mzimu woyera. (Machitidwe 1:4-5, 12-15; 2:1)

4.Kodi iwo anadzazidwa liti ndi mphamvu ya mzimu woyera?
Tsiku la Pentekoste, patangotha masiku khumi atakwera kumwamba. (Machitidwe 2:1-4)

5.Ndi ophunzira angati amene anadzazidwa ndi mphmvu ya mzimu woyera?
Ophunzira okwana zana limodzi ndi makumi awiri (120) omwe anasonkhana pamodzi. (Machitidwe 1:15; 2:1)

6.Kodi ophunzira anachita chiani atalandira mzimu woyera?
Ananenera za mphamvu ya zodabwitsa za Mulungu mziyankhulo zosiyanasiyana. (Machitidwe 2:4-12)

7.Kodi Ayuda osakhulupirira ananena chiani za ophunzira pamene anamva iwo akuyankhula ndi malilime ena?
Ananena kuti iwo aledzera ndi vinyo osasa. (Machitidwe 2:13-15)

8.Kodi Petro anaphunzitsa chiani pa Pentekoste?
Ananena kuti mzimu woyera unathiridwa ndi Ambuye woukitsidwayo monga mmene ananenera aneneri. (Machitidwe 2:16-21)

9.Kodi Petro anawauza chiyani anthu amene amamvetserawa?
"Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku chikhulupiriro cha machimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu woyera" (Machitidwe 2:38-39)

10.Ndi angati omwe anabatizidwa chifukwa cha uthenga wa Petro?
Pafupifupi anthu okwana zikwi zitatu (3000) anabatizidwa mu m'dzina la Yesu. (Machitidwe 2:41)

MAVESI OLOWEZA:
"Kristu anatiombola ku temberero la chilamulo, atakhala temberero m'malo mwathu; pakuti kwalembedwa, Wotembereredwa ali yense wopachikidwa pa mtengo; Kuti dalitso la Abrahamu mwa Yesu Kristu, lichitike kwa amitundu; kuti tikalandire lonjezano la Mzimuyo mwa chikhulupiriro." (Agalatiya 3:13-14)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 17
MPINGO WOYAMBA WA CHIPANGANO CHA TSOPANO
Machitidwe a Atumwi 3 – 4

1. Kodi mpingo unali bwanji patangodutsa Pentekoste?
Unapitirira m'chiphunzitso cha Atumwi ndipo unakula kwambiri. (Machitidwe 2:42-47)

2.Kodi kukula kwa mpingo mofulumiraku tinganene kuti chiani?
Ambuye anali kuonjezera tsiku ndi tsiku kuti anthu akapulumutsidwe. (Machitidwe 2:47b)

3.Kodi ndichozizwa chanji chimene chinachitika pa chipata cha mkachisi?
Kuchiritsidwa kwa munthu opuwala chibadwire. (Machitidwe 3:1-8)

4.Kodi munthu opuwala yemwe amakhala pa chipata cha kachisi anachiritsidwa bwanji?
Petro anamuuza iye,"M'dzina la Yesu mM'nazarayo yenda" (Machitidwe 3:6)

5.Kodi anthu anakhuzika bwanji ndi chozizwa cha machiritso a munthu opuwala uja?
Onse anali ozizwa ndipo anakhala chete namvetsera uthenga wa Petro. (Machitidwe 3:9-12)

6.Kodi Petro anafotokozera bwanji chozizwa cha machiritso a opuwala uja?
Ananene kuti chozizwa chimenechi chachitika ndi mphamvu ya Ambuye Yesu owukitsidwayo. (Machitidwe 3:12-16)

7.Kodi akuluakulu a Ayuda anakhuzika bwanji ndi uthenga wa Petro?
Anakwiya kwambiri ndipo anaika Atumwi m'ndende. (Machitidwe 4:1-3)

8.Kodi Petro ndi Yohane anawauza chiani akuluakulu amenewa tsiku lotsatira?
Kuti sangawaletse kulalikira m'dzina la Ambuye Yesu. (Machitidwe 4:18-20)

9.Kodi Atumwi anachita chiani pamene anawasiya kuti amuke mumtendere?
Anauza mpingo wonse za zomwe zinachitikazi. (Machitidwe 4:23)

10.Kodi Mulungu anayankha bwanji pemphero la mpingo?
Malo onse anagwedezeka ndipo anadzazidwa ndi mzimu woyera. (Machitidwe 4:31)

MAVESI OLOWEZA:
"Ndipo unyinji wa iwo akukhulupirira anali wa mtima umodzi ndi moyo umodzi; ndipo sanena mmodzi kuti kanthu ka chuma anali nacho ndi kake ka iye yekha; koma anali nazo zonse zodyerana. Ndipo atumwi anachita umboni ndi mphamvu yaikulu za kuuka kwa Ambuye Yesu ;ndipo panali chisomo chachikulu pa iwo onse" (Machitidwe 4:32-33)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 18
MAVUTO KU MPINGO WOYAMBA WA CHIPANGANO CHA TSOPANO
Machitidwe 5-7

1.Kodi tchimo linadziwika bwanji ku mpingo wa chipangano cha tsopano?
Hananiya ndi Safira ananama kwa Atumwi ndi Mulungu. (Machitidwe 5:1-4)

2.Kodi Hananiya ndi Safira analangidwa bwanji?
Anagwa pansi ndikufa pamapazi a Atumwi. (Machitidwe 5:5-10)

3.Kodi Mulungu anawonetsa bwanji mphamvu zake kupyorera mwa Atumwi?
Ambiri anachiritsidwa ku matenda ao kuphatikizapo iwo amene chithunzi cha Petro chinawakhuza . (Machitidwe 5:12-16)

4.Kodi akuru ansembe anakhuzika bwanji ndi zozizwa zimene Atumwi amachita?
Anakwiya kwambiri ndipo anaika Atumwi mundende. (Machitidwe 5:17-18)

5.Kodi Atumwi anapulumuka bwanji ku ndende?
Mngelo wa Ambuye anabwera ndikuwatsogolera iwo kunja. (Machitidwe 5:19-20)

6.Kodi Atumwi ananena chiani pamene anawauza kuti asalalikire mu dzina la Yesu?
Anawauza akuru a ansembe,"Tiyenera kumvera Mulungu koposa anthu" (Machitidwe 5:29)

7.Kodi ndi mavuto ati ena amene anabuka m'kachisi?
Ena mwa azimai chi Helenisite amasiye anaiwalika pa chitumikiro cha tsiku ndi tsiku. (Machitidwe 6:1)

8.Kodi ndi ofesi yanji imene Ambuye anaipereka kusamalira aumphawi?
Ofesi ya madikoni, yomwe amuna asanu ndi awiri anasankhidwa. (Machitidwe 6:2-6)

9.Kodi chinachitika ndi chiani kwa Stefano mmodzi mwa madikoni?
Ayuda osakhulupirira anatsutsana naye kuti akunyoza Mulungu ndipo anamugenda iye ndi miyala mpaka anafa. (Machitidwe 6:8-15; 7:54-60)

10.Kodi anali kuonerera ndani pamene Stefano anali kuponyedwa miyala?
Saulo wa kuTarisi yemwe patatha izi anali Mtumwi Paulo. (Machitidwe 7:58; 8:1a; 22:12-13, 20)

VESI LOLOWEZA:
"Mngelo wa Yehova azinga kuwachinjiriza iwo akuopa Iye, Nawalanditsa iwo" (Masalimo 34:7)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 19
MAZUNZO A MPINGO
Machitidwe 8 – 10

1.Kodi chinatsatira ndi chiani ataphedwa Stefano?
Kuzunzika kwakukulu kotsutsana ndi mpingo wa ku Yerusalemu. (Machitidwe 8:1)

2.Kodi zotsatira za chizunzo chimenechi ku mpingo chinali chotani?
Mpingo unabalalika kufikira ku Yudeya ndi Samariya. (Machitidwe 8:3-4)

3.Kodi anatumizidwa ku Samariya kukalalikira Uthenga Wabwino ndani?
Filipo, yemwe anali dikoni pa nthawi imeneyi. (Machitidwe 8:5-13)

4.Kodi chinachitika ndi chiani Filipo atatumizidwa ku Gaza ndi mzimu?
M'dindo wamphamvu wa Kandake wa ku Aitiopiya yemwe anatumidwa ndikubatizidwa ndi iye. (Machitidwe 8:26-38)

5.Ndi chifukwa chiani Saulo anapita ku Damasko?
Kuti akazunze okhulupirira kumeneko. (Machitidwe 9:1-2)

6.Chinachitika ndi chiani pamene Saulo anali paulendo wopita ku Damasko?
Ambuye owukitsidwa ndi okwezedwa anaonekera kwa iye. (Machitidwe 9:3-9)

7.Ndi chifukwa chiani Ambuye Yesu anaonekera kwa Saulo pa njira ya ku Damasko?
Amafuna kumusintha iye kuti akhale Mtumwi wogwira ntchito yotumikira Iye kwa amitundu. (Machitidwe 9:6,10-20)

8.Ndi masomphenya ati amene Ambuye anamuonetsa Petro ku Yopa?
Masomphenya a nyama zosadyedwa zikutsika mchotengera ngati chinsalu chachikulu. (Machitidwe 10:8-17)

9.Kodi tanthauzo la masomphenya amenewa a Petro ndi chiani?
Kuti Uthenga Wabwino ndi wa a mitundu komanso Ayuda omwe. (Machitidwe 10:15; 34-35; 15:6-7)

10.Ndi chifukwa chiani masomphenyawa anaonetsedwa kwa Petro?
Chifukwa anayenera kupita kwa Koneliyasi, yemwe ndi wa amitundu ku Kaesaleya Kuti akalalikire uthenga Uthenga. (Machitidwe 10:17-35)

VESI LOLOWEZA:
“Koma wina akamva zowawa ngati Mkristu asachite manyazi; koma alemekeze Mulungu m'dzina ili.” (1 Petro 4: 16)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 20
MPINGO WA KU ANTIYOKEYA
Machitidwe 11 – 12

1.Kodi ndichifukwa chiani mpingo wa kwa Antiokeya unali ofunika?
Chifukwa panali pakati pa zochitika za utumiki. (Machitidwe 11:20-27)

2.Anatumizidwa ku Antiyokeya kuchokera ku Yerusalemu ndani?
Barnabasi yemwe anagwira ntchito mopindila. (Machitidwe 11:22-24)

3.Kodi Herodi anayamba bwanji kuzunza mpingo pa nthawi imeneyi?
Anapha Mtumwi Yakobo ndipo anaika Petro mundende. (Machitidwe 12:1-5)

4.Kodi Petro anaphedwanso nthawi imeneyi?
Ayi, Ambuye anampulumutsa iye kundende. (Machitidwe 12:6-12)

5.Kodi Mulungu analanga bwanji Herodi woipayo?
Mulungu anatumiza mngelo ndi kupha iye ndipo anadibwa ndi mphutsi. (Machitidwe 12:23)

6.N'chifukwa chiani Ambuye analanga Herodi?
Chifukwa anali kuwauza anthu kuti iye ndi mulungu wao. (Machitidwe 12:19-23)

7.Kodi mpingo wa ku Antiyokeya unatthandiza bwanji okhulupirira a ku Yudeya?
Anatumiza ndalama kwa iwo panthawi yomwe kunali chilala. (Machitidwe 11:28-30)

8.Kodi tikuwerenga zotani za mpingo pa nthawi imeneyi?
Unakula ndikufala kupyolera mMawu a Mulungu. (Machitidwe 11:20- 24; 12:24)

9.Kodi Barnaba ndi Paulo anatengana ndi ndani kuchokera ku Yerusalemu?
Yohane Marko. (Machitidwe 12:25)

10.Anatumiza Paulo ndi Barnaba ku utumiki woyamba wa ulendo wao ndi ndani?
Mzimu Woyera kupyolera ku mpingo wa kwa Antiyokeya. (Machitidwe 13:1-4)

VESI LOLOWEZA:
"Koma inu ndinu m'badwa yosankhika, ansembe achifumu, mtundu woyera mtima, anthu a mwini wache, kotero kuti mukalalikire zoposa za Iye amene anakuitanani muturuke mumdima, mulowe kuunika kwake kodabwitsa" (1 Petro 2:9)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 21
ULENDO WOYAMBA WA UTUMIKI
Machitidwe 13 – 15

1.Kodi tinganene chiani za ntchito yonse ya Paulo?

Paulo nthawi zonse analalikira poyamba kwa Ayuda ndipo kenako analalikira kwa amitundu. (monga Machitidwe 13:42, 44-46; 14:1)

2.Kodi Paulo anatsutsana ndi ndani pa chisumbu cha Pafo?

Baryesu wamatsenga amene anakanthidwa ndi khungu kwa kanthawi. (Machitidwe 13:6-12)

3.Kodi Baryesu anatsutsa bwanji Paulo?

Anafuna kupatutsa kazembe asakhulupirire Yesu. (Machitidwe 13:8)

4.Kodi anamusiya Paulo ndi Banaba atafika ku m'Pisidiya ndani?

Yohane Mariko yemwe anabwerera kupita ku Yerusalemu. (Machitidwe 13:13)

5.Kodi ntchito ya mamishonare amenewa inali yosavuta?

Ayi, poti nthawi zambiri anali kuzunzidwa ndi Ayuda osakhulupirira. (Monga Machitidwe 13:45,50; 14:2-5,19)

6.Ndani anakhulupirira Uthenga wa Paulo ndi Banaba?

“Anakhulupirira onse amene anaikidwiratu ku moyo wosatha” (Machitidwe 13:48)

7.Kodi anthu anachita chiani ku Lustra pamene Paulo anachiza munthu opunduka miyendo chibadwire?

Anthu anayamba kupembeza Atumwi ngati milungu ya dziko. (Machitidwe 14:11-18)

8.Kodi Paulo ndi Barnaba anachita chiani atabwerera ku Antiyokeya?

Anayendera mipingo yonse anaikhazikitsa, ndikulimbikitsa miyoyo ya ophunzira ndipo anawayamikira kuti apitirize m'chikhulupiriro. (Machitidwe 14:26-28)

9.Kodi ndi mavuto otani amene anadza m'mipingo pakati pa Ayuda ndi a Khristu a mitundu?

Panali kusamvana pankhani za chilamulo ndi m'dulidwe mu mpingo. (Machitidwe 15:1, 5, 24)

10.Kodi mpingo unaganiza bwanji pa nkhani imeneyi pa nsonkhano omwe unachitika ku Yerusalemu?

Zoti a mitundu okhulupirira sanayenera kudulidwa. (Machitidwe 15:22-29)

VESI LOLOWEZA:

“Ndipo tidziwa kuti amene akonda Mulungu zinthu zonse zithandizana kuwachitira ubwino, ndiwo amene aitanidwa monga mwa kutsimikiza kwa mtima wache.” (Aroma 8:28)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 22
ULENDO WACHIWIRI WA UTUMIKI
Machitidwe 16

1.Kodi ndi chifukwa chiani Paulo ndi Barnaba sanathe kuyendera limodzi pa ulendo wao wachiwiri wa utumiki?

Chifukwa sanagwirizane zotenga Yohane wotchedwa Mariko paulendowo. (Machitidwe 15:36-40)

2.Kodi Paulo anapita yekha pa ulendo umenewu?

Ayi, Paulo anatenga Sila pamene Barnaba anatenga Yohane Mariko. (Machitidwe 15:39-40)

3.Kodi Paulo anatenganso ndani kuchokera ku Lustra?

Timoteo, yemwe anali wothandiza wokhulupirika. (Machitidwe 16:1-3; 1 Akorinto 4:17; ndi ena)

4.Kodi Paulo anaona chiani mumasomphenya ake ku Trowa?

Munthu anati, “Muolokere ku Makedoniya kuno, mudzatithandize ife”. (Machitidwe 16:9)

5.Kodi masomphenya a Paulo amatanthauza chiani?

Pakuti mzimu woyera umaitanira iwo kukalalikira Uthenga Wabwino ku Makedoniya. (monga Machitidwe 16:10-15)

6.Kodi otembenuka mtima oyamba ku Filipi anali ndani?

Lidiya, yemwe mtima wake Ambuye anautsegula. (Machitidwe 16:14-15)

7.Kodi Paulo ndi Sila anazunzidwa bwanji ku Filipi?

Anamenyedwa ndikuikidwa mu ndende pamene anachotsa mzimu wobwebweta wa namwali (Machitidwe 16:16-24)

8.Kodi chinachitika ndi chiani usiku uja pamene Paulo ndi Sila anali mu ndende?

Pamene Paulo ndi Sila anali kuimbira Mulungu nyimbo za matamando panali chivomerezi chachikuru pomwepo makomo a ndende anatseguka modabwitsa. (Machitidwe 16:25-28)

9.Kodi mdindo wa ndende anapempha chiani kwa Paulo ndi Sila?

Ambuye, “ndichitenji kuti ndipulumuke?” (Machitidwe 16:30)

10.Kodi Paulo anamuyankha chiani mdindo wa ku Filipi?

Ukhulupirire Ambuye Yesu ndipo udzapulumuka, iwe ndi apabanja ako. (Machitidwe 16:31)

MAVESI OLOWEZA:

“Odala ali akuzunzidwa chifukwa cha chilungamo;chifukwa uli wao Ufumu wa Kumwamba. Odala muli inu m'mene adzanyazisa inu, nadzazunza inu, nadzakunenerani monama zoipa ziri zonse chifukwa cha ine. Sekerani, sangalalani; chifukwa mphotho yanu ndi yaikulu m'Mwamba; pakuti potero anazunza aneneri anakhalawo musanabadwe inu”. (Mateyu 5:10-12)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 23
ULENDO WACHIWIRI WA UTUMIKI (KUPITIRIZA)
Machitidwe 17 – 18

1.Kodi Ayuda osakhulupirira amachita chiani ku Tesalonika?
Ayuda anatenga anthu ena oipa achabe a pabwalo nazunza Atumwi. (Machitidwe 17:1-9)

2.Kodi Paulo anapita kuti atachoka ku Tesalonika?
Anapita ku Bereya komwe okhulupirira analandira mau ndi kufunitsa kwa mtima wonse nasanthula m'malembo masiku onse ngati zinthu zinali zotero. (Machitidwe 17:10-12)

3.Ndi chifukwa chiani Paulo anachoka ku Bereya?
Ayuda oipa ochokera ku Tesalonika anabwera nausa, navuta makamu Kumeneko mosutsana ndi Iye. (Machitidwe 17:13-14)

4.Kodi anthu a Atene anaulandira bwanji uthenga wa Paulo?
Ambiri ananyoza pamene iye ananena za kuuka kwa akufa. (Machitidwe 17:15-20, 32)

5.Kodi anapita kuti atachoka ku Atene?
Anapita ku Korinto komwe anagwira ntchito kwa chaka chimodzi ndi theka. (Machitidwe 18:1, 11)

6.Kodi Akula ndi Priskila anali ndani?
Anali osoka mahema ku Korinto omwe Paulo anakhala nao. (Machitidwe 18:2-3)

7.Kodi ntchito ya Atumwi inapindula ku Korinto?
Inde, chifukwa Ambuye anali ndi osankhidwa ake ambiri mu mzindawu. (Monga Machitidwe 18:4-10)

8.Kodi ena mwa okhulupirira a ku Korinto anali ndani?
Krispo, mkulu wa wa sunagoge, ndi banja lake. (Machitidwe 18:8)

9.Kodi Paulo anapita kuti atachoka ku Korinto?
Anabwerera ku Yerusalemu, kudutsa m'madera ndi mizinda yambiri kuti akakhale pa mgonero wa pentekoste. (Machitidwe 18:18-23)

10.Kodi munganene chiani za ulendo wa utumiki wachiwiriwu?
Uthenga unafalikira ku Makedoniya . (monga Machitidwe 16:9; 17:1-15; 18:1)

VESI LOLOWEZA:
“Pakuti Uthenga Wabwino sundichititsa manyazi; pakuti uli mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu ali yense wakukhulupira kuyambira Myuda, ndiponso Mhelene” (Aroma 1:16)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 24
ULENDO WACHITATU WA UTUMIKI
Machitidwe 19 – 22

1.Kodi Paulo anatenga nthawi yayitali ya utumiki wake kuti?

M'zinda wa Aefeso, komwe anagwira ntchito kwa zaka zitatu. (Machitidwe 19:1, 8-10; 20:31)

2.Kodi Paulo analalikira kwambiri ku Aefeso?

Inde, ndipo anachitanso zodabwitsa zambiri. (Machitidwe 19:11-12)

3.Kodi uthenga wa chokhumudwitsa chomwe Atumwi anakumana nacho ku Efenso chinali chotani?

Anamva mavuto a ku mpingo wa ku Korinto. (Machitidwe 19:21-22; 1 Akorinto 1:11)

4.N'chifukwa chiani Paulo anachoka ku Aefeso?

Chifukwa Demetriyo wosula siliva anayambitsa phokoso. (Machitidwe 19:23 – 20:1)

5.Kodi Paulo anachita chozizwa chotani ku Trowa?

Anaukitsa mnyamata wakufa yemwe anagwa atakhala pazenera pasanja pachiwiri pamene Paulo anali kulalikira. (Machitidwe 20:6-12)

6.Kodi Paulo anakumana ndi ndani pa Mitelene?

Akulu akulu ochokera ku mpingo wa ku Aefeso. (Machitidwe 20:16-17)

7.Kodi Paulo anawachenjeza chiani akulu ampingo a ku Aefeso?

Kuti akawachokera iye mimbulu yosautsa idzalowa ndipo sizalekelera nkhosa iri yonse. (Machitidwe 20:18-35)

8.Kodi Agabu mneneri analosera chiani za Paulo?

Zoti Paulo adzamangidwa ndi Ayuda m'Yerusalemu. (Machitidwe 21:10-12)

9.Kodi Paulo amaopa kupita ku Yerusalemu?

Ayi, poti anati,"Pakuti ndakonzeka ine si kumangidwa kokha, komatunso kufera ku Yerusalemu chifukwa cha dzina la Ambuye Yesu" (Machitidwe 21:13)

10.Chinachitika ndi chiani ndi Paulo ku Yerusalemu pamene khamu la anthu anafuna kumupha?

Anapulumutsidwa ndi kapitao wamkulu wa Aroma. (Machitidwe 21:30-36)

VESI LOLOWEZA:

"Komatu sindichita manyazi; pakuti ndim'dziwa Iye amene ndamkhulupirira,ndipo ndikopeka mtima kuti ali wa mphamvu ya kudikira chosungitsa changacho kufikira tsiku lijalo" (2 Timoteo 1:12b)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 25
PAULO AYIKIDWA MUNDENDE KOMANSO ULENDO WAKE WA KU ROMA
Machitidwe 22 – 28

1.Kodi Paulo anakhalabe mundende ku Yerusalemu?

Ayi, anamutumiza ku Kaisareya, kuzemba chiwembu chofuna kumupha chomwe Ayuda anakonza. (Machitidwe 23:11-33)

2.Chinachitika kwa Paulo ndi chiani ku Kaisareya?

Paulo anamuzenga mlandu pamaso pa kazembe wotchedwa Felix. (Machitidwe 23:33 – 25:22)

3.Kodi Felix anasiya Paulo amuke mfulu?

Ayi, anazengedwanso kachiwiri ndi Mfumu Festo ndi Mfumu Agripa. (Machitidwe 25:23 – 26:32)

4**.N'chifukwa chiani Paulo anatumizidwa ku Roma?**

Chifukwa anachita apilu ya mulandu wake kuti ukakambidwe kwa Kaisara. (Machitidwe 26:32 – 27:1)

5.Kodi Paulo anazuzinzika bwanji paulendo wopita ku Roma?

Paulo anaponyedwa mmadzi ngalawa ikufuna kumira pa chisumbu cha Melita. (Machitidwe 27:37 – 28:1)

6.Kodi Paulo anachita chiani ali kapolo ku Roma?

Analalikira Uthenga wa Mulungu m'nyumba yache. (Machitidwe 28:30-31)

7.Kodi zotsatira za ulaliki wa Paulo ku Roma zinali zotani?

Anthu ena anakhulupirira kuphatikiza a mnyumba mwa Kaisara. (Filipo 1:12-13; 4:22)

8.Kodi Paulo ananyongedwa m'ndende panthawiyi?

Ayi, anatulutsidwa ndipo analemba mabuku a 1 Timoteo ndi Tito pa ulendo wake wa chinayi wa utimiki wake. (onani 1 Timoteo 1:3; 3:14; Tito 1:5; 3:12)[1]

9.Kodi Paulo anatsiriza bwanji utumiki wake?

Anaikidwa mundende ku Roma kachiwiri ndipo ananyongedwa atangolemba kumene buku la 2 Timoteyo (onani 2 Timoteo 1:16-17; 2:9)[2]

10.Kodi Mtumwi anatsiriza bwanji ntchito yake yonse monga kapolo wa Ambuye Yesu?

Ndipo anati,"Ndalimbana nako kulimbana kwabwino; ndatsiriza njirayo, ndasunga chikhulupiriro," (2 Timoteo 4:7)

MAVESI OLOWEZA:

"Popeza unasunga mau a chipiriro changa, Inenso ndidzakusunga kukulanditsa mu nthawi ya kuyetsedwa, ikudza pa dziko lonse lapansi, kudzayesa iwo akukhala padziko. Ndidza msanga; gwira chimene uli nacho , kuti wina angalande korona wako" (Chivumb 3:10-11).

[1] William Hendriksen, Atesalonika, Timoteo ndi Tito (Baker 1979), 25-28, 39-40
[2] Ibid, 40

Copyright © Gratia Dei Sola Media